

﴿هَلْ لَّكُمْ هُدًى﴾ ضَرَّالْأَفْلَحُ مَكْتُوعٌ وَيَوَّسُّلُ فِشْكَيْ وَهَادِدٌ إِذِ الرَّطْضُ مَلَأَ بِيْحِي نَمًا
نُورَكَ دَتَّ أَمَّ أَلِيْلَقَ

Kodi si Iye (Allāh) amene amayankha yemwe wasimidwa pamene wapanga du'ā komanso amachotsa choipa ndipo amakupangani inu kukhala oliyang'anira dzikoli? Kodi palinso mulungu wina pambali pa Allāh? Pang'ono pokha ndi pomwe mumakumbukira.

Adayankhula 'Ā'ishah kuti:[4]

عَشْرَ شَبَابٍ أَوْ سَيِّئًا مُّذُنًا لِّأَقْفٍ، إِنَّهُ كَلَّلَ نَعْمَ لَسَوْ هَلْ لَّيْلٍ صَّيِّبًا نُّنَا لِّسَانُ لِّأَسْ
لَّيْلٍ صَّيِّبًا نُّنَا لِّأَقْفٍ لِّأَقْفٍ. أَقْحُ نُّوْكَيَّ شَلَّابٍ نُّوْكَيَّ مُّذُنًا لِّأَقْفٍ، إِنَّهُ لَلَّ لِّأَقْفٍ رَّيَّ: أَوْلَاقُ
رَّيَّ لَوْنُ دُؤَايَ أَهْ رَقْرَقِيَّ يَّيَّ نُّجَّالٍ أَهْ طَحَّيَّ قَحَّ لَلَّ نُّمَّةً لِّلَّ كَلَّتْ: مَلَسَوْ هَلْ لَّ
بَدَّةً دَكَّةً نَّمَّ رَثَّ كَأَهْيَ فَنُطْلَحَّيَّ فَنُجَّاجٍ دَلَّةً رَقْرَقَكْ

Anthu ena adamufunsa Mtumiki wa Allāh (ﷺ) zokhudza aloseri (abimbi, asing'anga ngakhale abusa olosera), ndipo iye adati: "Alibe ntchito amenewo." Iwo (ma Swahābah) adati: "O iwe Mtumiki wa Allāh (ﷺ)! Zokamba zawo zina zimabweradi mu choonadi." Mtumiki wa Allāh (ﷺ) adati: "Liwu limene limakhaladi la choonadilo (kuchokera mu zokamba zawo) ndi lomwe Jinn loipa limalitenga mwa kuba (kuchokera kumwamba pamene angelo akukambirana) ndipo (Jinn limeneli) limalithira liwuli m'makutu a bwenzi lake (yemwe ali mloseriyo) kudzera mu kamvekedwe ka thazi (pamene Jinn likumuza munthuyo limamveka ngati nkuku yaikazi). Kenako mloseriyu amasakaniza ku liwuli bodza lokwanira zana limodzi (100)."

Izi ndi chisonyezo choti asing'anga sadziwa za kutsogolo ndipo ma Jinn amene amalumikizana nawowo za kutsogolo samazidziwa. Ndipo asing'anga alibe mphamvu zobweretsa vuto kwa munthu ngakhale kupereka phindu kwa munthu, kupatulapo kudzera mu chilolezo cha Allāh. Yemwe amabweretsa vuto kapena phindu kwa anthu ndi ziwanda ndi Allāh Yekha basi.

Chachiwiri, munthu amene wanamizidwa ndi asing'anga kuti achekeredwe mankhwala a mwayi kapena mangolomera, kapena achikondi ngakhale mankhwala ena alionsewo; iyeyu alape kwa Allāh kulapa kwenikweni. Chifukwa amakhala kuti watuluka mu chisilamu potengera hadīth ya Imran Ibn Huswayn yomwe Mtumiki wa Allāh (ﷺ) adayankhulamo kuti:[5]

هُوَ رَحْسٌ وَأَرْحَسٌ وَأَهْلٌ نَّهْكَتٌ وَأَهْلٌ رَّيَّطٌ وَأَهْلٌ رَّيَّطٌ نَمَّ أَنْ مَسَّيَ لَ.

Sali mwa ife yemwe amachita Tatwayyar[6] kapena kuchitiridwa Tatwayyar; kapena amachita maula kapena kuchitiridwa maula; kapena kuchita ufiti kapena kuchitiridwa ufiti (kukautenga ufiti kwa omwe amauchitawo).

Pambuyo polapa, sakuyeneranso kubwerera kwa asing'angawo kuti akamuchotse zomwe anamuchekerazo. Allāh ndi Yemwe ali ndi mphamvu yochotsa zimenezo ndipo lyeyo ndi Wakutha.

Allāh ndiye Mwini kuzindikira.

[1] Sūrah Al-Mā'dah 5:76

[2] Sūrah Az-Zumar 39:38

[3] Sūrah An-Naml 27:62

[4] Swahīh Al-Bukhārī, #7561

[5] Musnad al-Bazzār, #3578 (Swahīh li ghayrihi – Silsilat As-Swahīhah, #2195)

[6] Tatwayyar ndi mchitidwe wokhulupirira kuti mbalame zimabweretsa mwayi kapena tsoka